**Uthenga wochokera kwa wa pampando wa bungwe loyendetsa zisankho la Malawi Electoral Commission, Justice Dr Chifundo Kachale okhudza ndondomeko ya kaponyedwe ka voti pa chisankho chapadera cha pa 15 December, 2020**

Moni a Malawi anzanga.

Ndikuthokoza Mulungu chifukwa chotipatsa nthawi yabwino ino kuti tikambirane nkhani zokhudza kuponya voti pa zisankho zapadera zomwe zichitike lachiwiri pa 15 December, 2020 ku madera awa:

- Mangochi North East Constituency
- Mangochi West Constituency
- Phalombe North Constituency

Pachifukwa chimenechi ndikufuna kupereka uthenga wapadera ku dziko lonse, makamaka kwa anthu amene ali m'madera omwe muchitike zisankho zapaderazi. Ndondomeko yonse ili motere:

**Oyenera kuponya voti ndani?**

Oyenera kuponya voti ndiokhawo omwe analembetsa m'kaundula wa voti pokonzekera chisankho chapatatu mu 2019 ndipo ziphaso zao zovotera zikuyamba ndi "T19".

Malingana ndi chigamulo cha khoti cha pa 7 October 2020, magulu awiri awa ngakhale ali ndi ziphaso za voti kuchokera ku Malawi Electoral Commission sakuloledwa kuponya nao voti:

- Onse amene analembetsa pokonzekera chisankho chapadera cha pulezidenti chaka chino cha 2020 ndipo ziphaso zawo zimayambira "F20";
- Onse amene analembetsa mkaundula wa voti pokonzekera chisankho chapaderachi kuchokela pa 14 mpaka 27 September 2020 ndipo ziphaso zawo zovotera zikuyamba ndi "B20"

Kumbukirani kutenga chiphaso chanu chovotera popita kukavota. Ngati chinatayika, pitanibe kumalo omwe munalembetsera ndipo ogwira ntchito ya chisankho akayang'ana dzina lanu mkaundula wa voti. Dzina lanu likakapezeka adzakulolani kuti muponye voti.

**Ndondomeko yoponyera voti**

Malo oponyera voti adzatsegulidwa nthawi ya 6 koloko m'mawa ndikutsekedwa 6 koloko madzulo. Ngati pofika nthawi yotseka malo oponyera voti padzakhalebe anthu pa mzere, amenewo adzaloledwa kuponya voti, sadzabwezedwa.

Bungwe loyendetsa zisankho likukumbutsa anthu onse kuti, popita kukavota ndikoletsedwa kuvala, kunyamula kapena kupachika makaka aliwonse a chipani kapena a opikisana nawo pa chisankho. Mkulu oyang'anira malo oponyera voti wapatsidwa mphamvu

yochotsetsa wina aliyense opezeka atavala makaka a chipani ngati munthuyo sakuchotsa yekha. Amene adzapite kovota atavala za chipani adzabwezedwa kuti akasinthe ndi kubweranso bwino.

Mukafika kumalo oponyera voti mudzakhala pa mzere. Malo onse oponyera voti komwe kuli anthu oposera 1,000 m'kaundula adzakhala ndi mizere yoposera umodzi. Chonde kaonetsetseni kuti mwayima pa mzere oyenera malingana ndi dzina lanu. Ngati muli ndichikaiko, funsani oyendetsa chisankho kuti akulozereni mzere woti muyime. Nthawi yanu ikafika kuti mukaponye voti, ngati njira imodzi yopewera mlili wa Covid-19, dzasambeni m'manja ndi sopo pamalo osambira m'manja omwe bungwe loyendetsa zisankho layika pafupi ndi tebulo loyamba.

Mukafika pa kalaliki woyamba adzakupemphani kuti muonetse chiphaso chanu chovotera. Pofuna kupewa komanso kuchepetsa kufalikira kwa matenda a korona, chiphaso chanucho muzangomuonetsa kalalikiyu ndipo iyeyu adzawerenge chili m'manja mwanu. Kenako kalaliki adzayang'ana dzina lanu mkaundula wavoti. Dzina lanu ndi nkhope zikadzapezeka mkaundula wavoti, kalalikiyo adzayitana dzina lanu mokweza kuti anthu onse pamodzi ndi oyimira zipani adziwe amene akukavota.

Pamenepo mudzapita pa kalaliki wachiwiri amene adzapukute chala chanu chankomba phala chakumanja musanaviike mu inki. Inki imeneyi siyowopsya ku moyo wa munthu ndipo ndi chizindikiro chakuti munthu waponya voti.

Mukatero mudzapita pa kalaliki wachitatu pamene akakupatseni pepala lovotera (ballot paper). Ogwira ntchito ya chisankho adzakufotokozerani ndondomeko ya kavotedwe komanso kukuuzani mayina a anthu amene akupikisana nawo pa chisankho. Kuchoka apa mudzapita mu kachipinda komata m'mene mukakhalemo nokha kuti mukasankhe opikisana nawo wa ku mtima kwanu.

**Kusankha opikisana nawo pa chisankho**

Kuponya voti ndi kwa chinsinsi kotero musaope kapena kuopsyezedwa kuti mudzasankhe munthu amene simukumufuna. Posankha munthu mudzakhala nokha mu kanyumba komata ndipo palibe amene adzadziwe amene mwamusankha.

Kuti musankhe opikisana nawo muyenera kuchonga mu kabokosi kali kumanja kwa chizindikiro cha munthu amene mukumufuna. Onetsetsani kuti chochonga chanu chisatulukire kunja kwa bokosi limeneli. Ngati simungachonge muyenera kudinda ndi chala mkati mwa bokosi limeneli. Onetsetsani kuti musalipake inki pepala limeneli malo ena kupatulapo pamene mwadindapo. Ngati mwangozi inki yapakika malo ena osati amene mumafuna, dziwitsani ogwira ntchito pamalowo kuti akupatseni chipepala china chovotera ndipo choononongekacho muzabweza.

Mukasankha munthu amene mukumufuna, pindani pakati pepala la voti kuonetsetsa kuti mbali yovotera ili mkati. Pindaninso kachiwiri kenako ndi kukayiponya mu bokosi loponyera voti. Mukatero mwamaliza ndondomeko yonse yovota, sambaninso mmanja ndi

sopo ndipo nyamukani mudzipita kunyumba kuti mukadikire zotsatira. Simudzaloledwa kucheza kapena kumangozungulira pamalo oponyera voti.

Dziwaninso kuti ndikulakwira malamulo kuwulula munthu amene mukufuna kumuvotera kapena mwamuvotera chifukwa voti yanu ndi yachinsinsi. Simukuyeneranso kuonetsa kapena kupanga zizindikiro zoonetsa chipani chimene mumachikonda kapena opikisana nawo pa chisankho amene mumamukonda.

Komanso ndikulakwira lamulo kuwumiriza kapena kunyengerera munthu kuti awulule munthu amene wamuvotera. Aliyense akupemphedwa kuti adziwe za lamulo limeneli.

**Kaponyedwe ka voti kwa olumala**

Anthu onse olumala adzathandizidwa mwachangu ndipo sakuyenera kuyima nawo pa mzere. Anthuwa akafika pamalo oponyera voti akuyenera akadzionetse kwa oyendetsa chisankho amene adzawathandize kukawakhazika patsogolo.

Chimodzimodzinso kwa amayi oyembekezera, anthu okalamba ndi odwala onse adzathandizidwa msanga. Kwa anthu olumala amene

amayenda panjinga asade nkhawa popeza adzathandizidwa kuti aponye voti popanda kutsika pa njinga zawo. Kwa olumala m’njira zosiyanasiyana monga kumva kapena kupenya: lamulo likuti anthu oterewo adzabwere ndi munthu amene akumukhulupirira komanso akhale wakuti analembetsa nkaundula wa voti. Munthu ameneyu ndi

amene adzawathandize kuponya voti. Ngati sabwera ndi munthu owathandiza, lamulo limanena kuti: mkulu woyang'anira chisankho pa malopo atha kumuthandiza munthu oteroyo.

Pamenepa ndikupempha ma "monitala" onse kuti adzathe kumvetsetsa ndi kutsatira zimene lamulo limanena. Nthawi zina pamakhala kusamvetsetsa kukabwera munthu otereyo chifukwa ma monitala amafuna kuti akaone nawo kuti akumusankhira molondola kapena ayi. Izi zimafafaniza chinsinsi chavoti ndipo ndizoletsedwa m'malamulo.

Pambali pa zimene malamulo akunena, bungwe loyendetsa zisankho lapanga chikombole chomwe chidzathandize kuti anthu amene ali ndi vuto lopenya kuti avote osathandizidwa ndi munthu wina. Pogwiritsa nchito chikombole chimenechi anthu osaona adzatha kusankha wopikisana nawo pa chisankho wakumtima kwawo pogwiritsa ntchito zala zawo. Anthu awa akadzafika polandira mapepala ovotera, kalaliki adzawapatsanso chikombole chimenechi ndi kuwafotokozera m'mene angakagwiritsire ntchito kuti avote. Akatero adzatsogoleredwa kukanyumba komata komwe adzakasankhe munthu wa kumtima kwawo mwa iwo wokha.

**Ngati chiphaso cha voti chatayika kapena kuonengeka**

Aliyense okavota akupemphedwa kuti adzakumbukire kunyamula chiphaso chovotera. Kwa amene adataya ziphaso zawo, kaya zinabedwa, kuonongeka, kapena kulandidwa, ali ololedwa kuponya voti ku malo amene adalembetsera mayina awo mkaundula wa voti.

Akakafika pamalo ovotera ayenera kukadziwitsa oyendetsa chisankho kuti anataya chiphaso chawo. Pamenepo dzina lawo lidzafufuzidwa mkaundula wavoti. Ngati lapezeka adzaloledwa kuvota. Ngati dzina lawo lasowa, sadzaloledwa kuponya voti chifukwa umboni owonetsa kuti analembetsa palibe.

## Chitetezo pa malo oponyera voti

Bungwe la MEC lakhazikitsa chitetezo chokwanira. Kumalo onse oponyera voti kudzakhala a Polisi omwe ntchito yawo ndi kusungitsa bata ndi mtendere, pamene chisankho chikuchitika.

Ndichenjeze wina aliyense amene angakhale ndi maganizo ofuna kusokoneza zisankho pamene zili mkati; A Polisi adzakhala tcheru ndipo adzathana ndi wina aliyense oyambitsa ziwawa.

## Ngati kungagwe mvula

Tili mu nyengo ya mvula. Malingana ndi ndondomeko zathu zoyendetsera chisankho timayenela kuvotela pa bwalo. Koma ngati kungapezeke kuti kwabwera mvula pamene voti isanayambe, malo oponyera voti adzakhazikitsidwa mkati mwa makalasi. Ngati palibe makalasi, bungwe loyendetsa zisankho lidzapeleka zihema m’mene anthu adzaponyelemo voti.

Ngati mvula ingabwere kuponya voti kuli mkati, kuponya voti kudzayima kaye ndi cholinga chakuti asamutsile katundu mkati. Akangomaliza kusamuka, kuponya voti kuyenela kuyambiranso.

Ndilimbikitse anthu onse kupita kukaponya voti ngakhale kuti kukubwera mvula. Voti yanu ndi yofunika kwambiri.

Kwa onse oyimilila zipani ndi opikitsana nao (mamonitala), akuyenela kukhala mkati mwakalasi pamene kuponya voti kukuchitikila mkalasi. Monga mwa ndondomeko, chipani kapena opikisana wina aliyense akuyenela kukhala ndi oyimilira m'modzi pa nyengo iliyonse.

**Pempho kwa atsogoleri**

Mafumu ndi atsogoleri onse muli ndi udindo waukulu olimbikitsa anthu anu kuti adzapite kukaponya voti kuti adzasakhe munthu owayimirira.

Mafumu ndi atsogoleri amipingo musakondere chipani kapena wina aliyense amene akupikisana nawo pa chisankho.

Kwamakolo ndi aphunzitsi alimbikitseni ana anu omwe analembetsa kuti adzaponye voti yawo, pakuti ichi ndicho cholinga cholembetsera mkaundula wa voti.

Kwa olemba ntchito, ndikukupemphani kuti mudzawalore anthu anu onse amene adalembetsa mkaundula kuti adzapite kukaponya voti yawo monga njira imodzi yokwaniritsira ufulu wawo.

**Pempho la bata ndi mtendere**

Ndikulimbikitseni a Malawi amzanga kuti tisunge bata ndi mtendere pomwe mavoti adzakhale akuwerengedwa komanso zotsatira kuwulutsidwa. Ngati munthu adzakhale ndi dandaulo lirilonse lokhudzana ndi chisankho akalipeleka kwa mkulu oyendetsa

chisankho pa malo a voti omwe muli nao pafupi kapena kwa Bwana Mkubwa wa boma lanu. Iwowa adzakuthandizani moyenera ndithu.

**Kuwerenga mavoti**

Kuwerengera mavoti kudzayambika nthawi imene kuponya mavoti kwatha. Palibe bokosi limene lidzachoke pa malopo mavoti asanawerengedwe. Oyendetsa chisankho pa malowo ndi anthu okhawo amene adzaloledwe kuwerengera mavoti, ma monitala adzakhalepo panthawiyi kuti adzaonenerere kuwerenga kwa mavotiko.

Dziwani kuti mzere uli onse udzawerengera mavoti paokha ndipo pomaliza mkulu woyendetsa chisankho pa mzere umenewo adzanyamula zotsatira ndi kukapereka ku ofesi ya kwa Bwana Mkubwa wa boma limenelo.

“Monitala” aliyense ayenera kutsimikizira zosatira zonse za pa malopo posayinira ndipo ayenera kukhala ndi zotsatira zofanana ndizomwe zidzatumizidwe ku malo owonkhetsera mavoti. Zotsatirazi adzadzikhoma pamalo pamene voti idzachitikire kuti anthu onse adzathe kuona momwe voti yayendera pa malo pamenepo.

Ndipemphe azipani ndi omwe akuyima nawo pazisankhozi kuti awayang’anire mamonitala bwino lomwe kuti adzadzipereke pogwira ntchitoyi. Ma “monitalawa” alimbikitsidwe kuti asadzachoke pa malo oponya mavotiwa mpaka zotsatira zonse zitawerengedwa ndikusayinidwa. M’mbuyomu taonapo ma “monitala” akuchoka pamalo oponya mavoti pachifukwa choti munthu wawo sakuchita

bwino pa chisankho. Titsindike kuti siudindo wa “monitala” kupambanitsa opikisana nawo, koma ntchito yake ndi kuonetsetsa kuti zonse zikuyenda mwa dongosolo.

Bungwe loyendetsa chisankho likuyembekeza kuti lidzaulutsa zotsatira lachitatu pa 16 December, 2020 zonse zikayenda bwino.

**Kupewa matenda a Covid 19**

Bungwe loyendetsa zisankho likukumbutsa anthu onse kuti mlili wa Covid-19 udakalipobe. Chonde pamene mukupita kukavota lachiwiri lino pa 15 December onetsetsani kuti mukutsatira ndondomeko zonse zodzitetezera kutenga ka chirombo ka korona. Njira zake zina nazi;

- Popita koponya voti onetsetsani kuti mwavala mask kapena chotchinga pakamwa ndi pamphuno. Ngati kuli kotheka zatengeni mankhwala opaka mmanja, kapena kuti hand sanitizer. Komanso ngati nkutheka tengani cholembela chanu.

- Mukafika pa malo oponyera voti onetsetsani kuti mwayima motalikirana mikono iwiri ndi ena. Musapereke moni wa pa manja pamene mwakumana ndi achibale kapena anzanu.

- Pa malo a voti pakakhala madzi osamba m’manja komanso sopo. Mukasamba m’manja onetsetsani kuti mwaumitsa bwinobwino.

- Chiphaso chanu musadzapereke kwa woyendetsa chisankho koma mudzamuonetse ndipo adzawerenge dzina lanu ndi kuona nkhope yanu mutachigwira nokha chiphasocho.

- Onetsetsani kuti pali mpata okwanira pakati pa inu ndi ogwira ntchito ya chisankho komanso oyang'anira chisankho.

- Mukaponya voti yanu kumbukirani kusamba m'manja ndikubwerera kwanu.

Mulungu akudalitseni pomwe mukukaponya voti yanu la chiwiri lino pa 15 December, 2020.

Zikomo